NDIPO MASO AWO ANATSEGUKA NDIPO IWO ANAMUDZIWA IYE

Mu Uthenga wa Luka Woyera, ndipo kuyambira ndi mutu wa 24 ndi ya sarte-. . . ndime ya 31, kapena ine nditi ndime ya 30 ya mutu wa 24.

> *Ndipo zinachitika kuti, pamene iye anakhala pa chakudya ndi iwo,* ndipo *iye anatenga mkate, ndipo anaudalitsa iwo, ndipo anawunyema* iwo*, ndipo anawupereka kwa iwo.*
>
> *Ndipo maso awo anatseguka, ndipo iwo anamudziwa iye; ndipo iye anachoka pamaso pawo.*
>
> *Ndipo iwo anati kwa wina ndi mzake, Kodi* mitima *yathu siinatenthe mkati mwathu, pamene iye amayankhula ndi ife mphepete, mwanjira, ndi pamene iye amatsegula kwa ife malemba?*

2 Ndipo Ambuye awonjezere madalitso Ake. Phunziro langa likhala, ngati ine ndingalitchule ilo usikuuno: *Ndipo Maso Awo Anatseguka Ndipo Iwo Anamudziwa Iye*. Tsopano kwatentha, koma ine ndikukhumba inu mukadapirira momwe inu mungathere, kwa mphindi pang'ono chabe, ndipo ine ndiyesetsa kuti ndifulumire. Koma tsopano ife tikufuna tiyang'ane mwaulemu pa Mawu, Mawu a Mulungu odabwitsa. Ndipo ife tikupemphera kuti Mulungu, mwa njira inayake, atsegule maso athu usikuuno.

3 Ngati Isitara ili chikondwerero chabe cha chochitika cha mbiriyakale, ndipo icho chokha, ndiye ife tingakhale ndi chifukwa pang'ono kuti tikaikire, ife tingakhale ndi chifukwa pang'ono kuti tikhale ndi funso, chifukwa izo zingasiyidwe pa lingaliro laulemu longotenga zoyankhula. Ndipo ngati Khristu akanati sanapange malonjezo amene Iye anapanga, ndiye kuti nafenso, sibwenzi tiri ndi umboni umene ife tiri nawo.

4 Koma Ambuye wathu wodala anati, pamene Iye anali kuno pa dziko lapansi, "Kanthawi pang'ono, ndipo dziko silidzandiwonanso Ine." Tsopano mawu akuti *dziko* pamenepo, akuchokera ku "dongosolo la dziko, anthu a mdziko lapansi." "Dziko silidzandiwonanso Ine. Komabe inu mudzandiwona Ine, pakuti Ine ndidzakhala ndi inu, ngakhale mwa inu, mpaka kumathero a dziko lapansi." Tsopano, Mawu amenewo ndi owona basi monga Mawu ena aliwonse amene ife tawayankhula kudutsa msabata ino, kuchokera mu Baibulo, owona basi monga Mawu ena aliwonse mu Baibulo. "Kanthawi pang'ono, ndipo dziko silidzandiwonanso Ine. Maso awo sadzatsegulidwa

nkomwe." Alipo anthu amene anabadwa mdziko lapansi, osati mwa chifuniro cha Mulungu, koma mwachifuniro chawo chomwe cha umbombo sangakhoze kumukhulupirira Iye ngati Iye atati akuima pomwe pano akuyankhula ndi inu usikuuno. Ndi zachisoni kuti unene, koma Baibulo linanena kuti, "Iwo anabadwira mu dziko lino, ku chiwonongeko ichi," Yuda, ndipo pafupifupi ndime ya 3.

5 Tsopano, koma kwa inu, usikuuno, amene mumatuluka ndikudzaima mozungulira mchipinda, ndi kudzadzana pamodzi mu chipinda chaching'ono chotentha ngati ichi, inu simumangobwera kuti mudzawonedwe. Inu mumabwera kwa cholinga china. Ndipo, mwa kuganiza kwanga, inu mwabwera ndi kuwona mtima kwa mtima wanu, kuti mudzayende pafupi ndi Mulungu, kuti muchoke pano, usikuuno, munthu wabwinoko kusiyana ndi mmene inu munaliri pamene inu mumalowa muno. Ndi chimene ine ndimapemphera pamene ine ndimalowa pakhomo, usikuuno, "Ambuye, ndipangeni ine ndikhale munthu wabwinoko pamene ine ndizituluka, usikuuno, kusiyana ndi momwe ine ndikulowera." Tsopano pamene Iye . . .

6 Kuchoka Kwake kusanachitike, Iye ananena maneno a mtundu uwu. Iye anati, "Iye amene akhulupirira pa Ine . . ." Yohane Woyera, mutu wa 14, ndime ya 7. "Iye amene akhulupirira pa Ine, ntchito zimene Ine ndikuzichita nayenso adzazichita; zoposa izi iye adzazichita, pakuti Ine ndikupita kwa Atate Anga. Ine ndikupita, ndipo ndidzabweranso."

7 Tsopano ife tikupeza kuti ntchito zimene Iye ankachita. Ntchito zimene Iye ankachita? Iye sanali kudzinenera kuti anali munthu wamkulu, Iye anangokhala Munthu wodzichepetsa basi. Iye samayankhula ndi mawu aliwonse apamwamba, Iye amangoyankhula ngati Munthu wamba. Iye amakhala pakati pa osauka, "nkhandwe zinali ndi mauna, ndipo mbalame zinali ndi zisa, koma Iye analibe malo oti agonekepo mutu Wake." Iye anali ndi chovala chimodzi, chimene chinapatsidwa kwa Iye, "icho chinali chonse choluka, chinalibe msoko pa icho."

8 Ndi chifukwa chake iwo anachitira maere pa icho. Nchifukwa chiyani zinatero? Chifukwa ulosi wa Chipangano Chakale umayenera kuti ukwaniritsidwe, "Iwo anagawana zovala Zanga, anapanga maere pa chovala Changa." Chotero iwo sakanatha kuchigawaniza icho pa msoko, iwo anachita kuchichitira juga icho, ndipo izo zinali kuti akwaniritse ulosi wa Chipangano Chakale.

9 Koma ife tizindikira, mu pafupifupi mphindi pang'ono chabe, Iye anachita chiyani? Ndipo ine ndikukhulupirira, usikuuno, ndi njala ya uliwonse wa mitima yathu, kuyambira kwa wamng'ono kupita kwa wamkulu, usikuuno, kuti timuwone Yesu Khristu. Icho ndi chokhumba cha mtima wanga. Ndipo

nchifukwa chiyani ziri chomwecho? Ngati ife timadzinenera mwa Malemba . . .

10 Mawailesi akulengeza izo lero, matelevizioni aziyika izo pa zochitika, zisudzo zanenapo, kuti, "Iye sali pano, koma Iye wauka!"

11 Chabwino, ndiye, ngati Iye wauka, Baibulo linanena, mu Ahebri 13:8, "Iye ali yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse." Tsopano, apa ndi pomwe izo ziri, anthunu. Icho mwina ndi Choonadi, kapena icho si Choonadi. Kuti, ngati icho sichiri Choonadi, ndiye kuti Baibulo ndi labodza, ndiye kuti Mawu ndi abodza; ndiye kuti ife tataika, ndipo palibeponso chiukitsiro cha akufa, ndipo ife tikungozipangitsa kukhulupirira. Koma ngati icho chiri Choonadi, ndiye Icho chikuyenera kuzitsimikizira Chokha.

12 Ngati inu mutanena kuti madzi awa ndi onyowa; ine sindinayambe ndawawonapo madzi. Inu mukawatsanulira iwo pa ine, ndipo nkukhala kuti si onyowa, ndiye anu—mawu anu si owona. Koma ngati mutawatsanulira iwo pa ine, ndipo iwo nkukhala onyowa, ndiye kuti mawu anu ndi owona.

13 Ngati Khristu ali yemweyo dzulo, lero ndi kwanthawizonse, ndiye kuti Baibulo ndi lowona. Ngati Iye sali yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse, ndiye kuti Ilo si lowona. Ngati Mawu a Mulungu sali owona, ndiye kuti Khristu si wowona. Ndiye, ngati Mawu a Mulungu si owona, Mulungu si wowona. Koma, ndiye, ngati Mawu a Mulungu ali owona, ndiye kuti Baibulo ndi lowona, Mulungu ndi wowona, Khristu, ndi wowona, ndipo ife tikuyenera kukhala owona kwa Cholingacho. Kulondola!

14 Tsopano, pamene Iye anali pa dziko lapansi, Iye sanali kudzinenera kukhala mchiritsi wamkulu aliyense. Ndi angati akudziwa kuti Mwana wa Mulungu samadzinenera kuti anali mchiritsi? [Osonkhana akuti, "Ameni."—Mkonzi]. Kulondola ndendende. Iye anati, "Ine sindingathe kuchita kanthu mwa Inemwini, koma chimene Ine ndiwona Atate akuchita. Si Ine amene ndikuchita ntchitozi," Iye anati, "ndi Atate amene akukhala mwa Ine. Iye akuchita ntchitozo." Iye amachita ntchito za mtundu wanji?

15 Ife tikupeza mu Baibulo, pamene munthu wa dzina lake Filipo anapulumutsidwa. Ndipo iye anapita ndipo anakamupeza mzake, Natanieli; kutali mmbuyo, mamailosi sarte kuzungulira phiri. Iye anamubweretsanso iye kwa Yesu. Ndipo pamene iye anamupeza iye, iye anali pansi pa mtengo, akupemphera. Ndipo iye anati, "Bwera, udzawone Yemwe ife tamupeza; Yesu wa ku Nazareti, mwana wa Yosefe."

Iye anati, "Pangakhale chirichonse chabwino kuchokera mu Nazareti?"

Iye anati, "Bwera ndipo udzawone."

16 Ndiwo umboni wabwino umene ine ndikuwudziwa.
Musatenge mawu a munthu wina aliyense pa Izo. Bwera,
udzadziwonere wekha! Anati, "Bwera ndipo udzawone."

17 Ndipo pamene iye anabwera, Yesu anali ataima pa mzere,
mwinamwake akuwapempherera anthuwo. Ndipo pamene
Filipo anabwera, ndi Natanieli, Yesu anati, "Taonani mu Israeli,
mwa yemwe mulibemo chinyengo!"

18 Iye anati, "Ndi liti limene inu munandidziwa ine, Rabbi?" Izo
zinamudzidzimutsa iye. "Inu mwandidziwira ine kuti?"

19 Iye anati, "Filipo asanakuitane iwe, pamene iwe unali pansi
pa mtengo, ine ndinakuwona iwe." Kutali mamailosi sarte,
kudutsa phiri, komabe, "Ine ndinakuwona iwe."

20 Izo zinawonetsera Yemwe Iye anali. Iye anali Mulungu
wopezekaponseponse; osangoti mneneri, koma Mulungu
Iyemwini anawonetseredwa mu thupi. Ndi chifukwa chake Iye
anatha kuwuika iwo, moyo Wake, pansi, nkudzawutenganso iwo
kachiwiri.

21 Mkazi wamng'ono anatulukira kuti adzatunge madzi tsiku
lina. Ndipo Iye anayankhula ndi iye, ndipo anati, "Mkazi,
ndibweretsere Ine akumwa!"

22 Iye anati, "Si mwambo wake kuti inu Ayuda mutifunse ife,
Asamariya, zoterozo. Ife sitimachitira zinthu limodzi wina ndi
mzake."

23 Iye anati, "Koma ngati iwe ukanadziwa Yemwe iwe
ukuyankhula naye, iwe ukanandipempha Ine akumwa. Ine
ndikanakupatsa iwe Madzi amene iwe sumabwera kuno
kudzatunga."

24 Ndipo iye anati, "Chitsimechi ndi chakuya, Bwana. Inu
mulibe choti mutungire nacho, ndipo kodi Madzi amenewa Inu
mukawatenga kuti."

25 Kodi Iye anali kuchita chiyani? Kuwukhudza mzimu wake.
Ndipo pamene Iye anapeza chimene chinali vuto ndi iye,
vuto lake linali lakuti iye anali kukhala mu chigololo. Iye
anali ndi amuna asanu, ndipo amakhala ndi wa chisanu ndi
chimodzi wake.

Ndipo Yesu anati kwa iye, "Pita, ukamutenge mwamuna
wako, ndipo ubwere naye kuno."

Ndipo iye anati, "Ine ndiribe mwamuna aliyense."

26 Iye anati, "Ayi, iwe wakhala nawo asanu, ndipo mmodzi
amene iwe ukukhala naye tsopano si wako. Chotero, iwe wanena
bwino."

27 Taonani tsopano, Myuda. Pamene Yesu anachita chozizwitsa
chimenecho kwa iye, Myuda wokhazikika weniweni ameneyo,
weniweni, Myuda woona, anati, "Inu ndinu Mwana wa Mulungu,

Mfumu ya Israeli." Iye anadziwa kuti zizindikiro zimenezo zikuyenera kumutsatira Mesiya.

28 Ndipo tsopano apa pali Msamaria. Pamene chozizwitsa chimenecho chinachitika pa iye, iye anati, "Bwana, ine ndazindikira kuti Inu ndinu Mneneri. Ife tikudziwa kuti pamene Mesiya adzabwera, Iye adzatiuza ife zinthu izi. Koma Inu ndinu Ndani?"

Iye anati, "Ine ndine Iye yemwe akuyankhula ndi iwe."

29 Iye anasiya mtsuko wake wamadzi, ndipo anathamangira mu mzinda, ndipo anati, "Bwerani, mudzamuwone Munthu Yemwe wandiuza ine zinthu zimene ine ndachita. Kodi ameneyu si Mesiya yemwe?" Ndithudi.

30 Kumapitirira kudutsa Malemba ife tikhoza kuzitenga izo, momwe Iye amachitira zinthu zimene Atate ankamuwonetsera Iye. Baibulo linanena, mu Yohane Woyera, pamene iwo anamufunsa Iye zokhudza chifukwa chimene Iye sanachiritsire anthu opuwala onse aja, ndipo Iye anati, "Indetu, indetu, Ine ndinena ndi inu." Yohane Woyera 5:19, "Indetu, indetu, Ine ndinena ndi inu, Mwana sangachite kanthu mwa Iyeyekha; koma chimene Iye awawona Atate akuchita, chimenecho amachita Mwana chimodzimodzi."

31 Tsopano, ngati Khristu wauka kwa akufa, ndipo ali pakati pathu lero; ndipo analonjeza kuti zinthu zomwezo zimene Iye anazichita, kuti tikanazadzichita ifenso; ndizo mwina Choonadi, kapena izo si Choonadi. Baibulo linati, "Iye ali yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse."

32 Ndipo, abwenzi, ndine wokondwa basi kudziwa, lero, kuti ine moonadi, ndi zonse zimene ziri mkati mwanga, ndikukhulupirira kuti Yesu Khristu ndi Mwana wa Mulungu. Iye anakhalitsidwa mchiberekero ndipo anabadwa, kubadwa kwachiyero. Iye anazunzika pansi pa Pontius Pilato; anapachikidwa, anafa, anaikidwa mmanda, anaukanso tsiku lachitatu; ndipo anakwera kupita Kumwamba, ndipo akukhala pa dzanja lamanja la Ufumu Wake. Ndipo Mzimu Woyera uli pano ukupitiriza ntchito yomweyo imene Iye anaichita pamene Iye anali kuno pa dziko lapansi. Ndi ganizo lokongola bwanji!

33 Ndi mmawa wokongola bwanji, mmawa woyamba wa chiukitsiro, Isitara yoyamba imene inayamba yatulukirapo pa dziko lapansi! Kodi inu mukuzindikira kuti Isitara iyi imene ife tikuikondwererayi, ya chiukitsiro Chake, ikungotilozera ku Isitara yaikulu imene ikubwera, ora limene Iye azidzabwera kuchokera Mmiyamba? Ndipo onse amene anafa mwa Khristu adzawuka ndipo adzapita ndi Iye. Ife tikungoyembekezera zimenezo, Isitara yaikulu, ikubwera. Ndipo, lero, ndi zokongola bwanji zimenezo, ndi chitonthozo bwanji, ndi chitsimikiziro bwanji chimene ife tiri nacho, pamene Baibulo likudzinenera izo, pamene kupezekaponseponse Kwake kukudzinenera izo,

pamene Mphamvu Yake yamachiritso ikudzinenera izo, pamene Mzimu Wake waukulu ukudzinenera izo, pamene chirichonse mu chirengedwe chikudzinenera izo, Mpingo Wake ukudzinenera izo, mtima wanga ukudzinenera izo, mtima wa munthu aliyense wobadwanso mwatsopano ukudzinenera zimenezo, kuti, "Yesu Khristu ndi Mwana wa Mulungu, ndipo adzabweranso! Ndipo Iye ali yemweyo tsopano, 'Dzulo, lero, ndi kwanthawizonse!'" Tsopano zindikirani.

34 Unali mmawa wokongola wa Isitara uwu. Panali patakhala mphekesera zochuluka, zikuyankhulidwa. Akazi ena anali atabwerera kuchokera ku manda, ndipo anati iwo anawona masomphenya a Angelo. Ndipo iwo amaganiza kuti anali wosamalira maluwa; Maria, amake, pakuti iye anamva liwu likuyankhula kumbuyo kwake, ndipo linati, "Inu mukufuna Ndani?" Ndipo pamene Iye anapotoloka . . .

35 Iye anapotoloka, ndipo anati, "Iwo adzamutenga Ambuye wanga. Ine sindikudziwa kumene iwo akamugonekako Iye. Ngati Inu mukudziwa, ndiuzeni ine kumene Iye ali, ndipo ine ndipita ndikamutengeko Iye."

Iye anapotoloka, ndipo anati, "Maria."

36 Ndipo iye anamuyang'ana Iye, ndipo iye anati, "Rabboni," kutanthauza, "Ambuye!"

37 Iye anati, "Usandigwire Ine, pakuti Ine sindinakwere panobe. Koma Ine ndikwera kwa Atate ako, ndi kwa Atate Anga; kwa Mulungu wanga, ndi kwa Mulungu wako. Koma pita, ukawauze akuphunzira Anga Ine ndikakumana nawo iwo ku Galileya."

38 Momwe izo zinkawonekera ngati nthano zopanda pake, za Munthu uyu amene iwo anamuwona ali mtembo; ndipo anafa, anaikidwa mmanda, ndipo ili linali tsiku lachinai, kapena lachitatu Iye atafa. Petro anali atakhumudwa, ndipo ankafuna kuti azipita kukawedza. Awiri a iwo anati, mmodzi dzina lake Kleopa, anati, "Ife tingobwerera kwathu, ku Yerusalemu." Ndipo ali pa njira yawo, akuyenda, mmawa umenewo. Pamene Petro anatenga mbedza yake yowedzera ndipo nanyamuka, wokawedza. Awiri awa anali pa njira yawo, achisoni. Ndipo pamene iwo amayenda pa njira yawo, akuti, "Chabwino, ine ndikuganiza moyo si woyenera kukhalidwa. Oh, momwe ife timakhulupirira kuti Iye anali Mesiya! Zinatheka bwanji Munthu uja, Yemwe amaukitsa akufa, kuima nkumusiya wansembe wamkulu uja amuseleule Iye? Zinatheka bwanji Munthu uja, Yemwe amatha kuwona masomphenya pambuyo pa masomphenya, angamulole bwanji msilikari wachi Roma kuika chiguduli pa nkhope Yake, ndi kumumenya Iye pa mutu, ndi kuti, 'Ngati Iwe uli mneneri, tiuze ife yemwe wakumenya Iwe'? Zinatheka bwanji kuti Iye anafuulira chifundo, pa mtanda,

powona kuti Iye amatha ngakhale kuwukitsa akufa?" Oh, inali nthawi yokhumudwitsa!

39 Ndipo nthawi zokhumudwitsa zimenezo zimabwera kwa wokhulupirira aliyense, kuti akuyese iwe, ndi kudzakuyesa iwe, ndi kudzawona ngati iwe ukukhulupirira zenizeni. "Mwana wamwamuna aliyense amene amabwera kwa Mulungu, amayenera ayesedwe kaye poyamba, mwana-wophunzitsidwa."

40 Padzakhala ena a inu pano usikuuno, sindikukaikira, adutsa mukuyesedwa komweko. Ngati ife tingaitane mzere wa pemphero, ine sindikudziwa nndani ali ndi makadi a pemphero, palibe mmodzi aliyense akudziwa; iwo anangosakanizidwa onse pamodzi, ndipo anaperekedwa kwa inu. Ine ndiitana kuyambira penapake, paliponse pamene pangakhale pa mtima panga pa nthawiyo. Ife sitingakhoze kukwanitsa koma apang'ono pa nthawi. Madazeni angapo, mwinamwake, adutse pa mzere wa pemphero. Onse akufuna kuti abwere. Inu mukhoza kuganiza kuti Iye wakudutsani inu, koma Iye sanatero. Iye akungokuyesani inu, akungofuna kuwona ngati inu mukumukhulupirira Iye kwenikweni. Masomphenya samachiritsa; masomphenya amangotsimikizira Kukhalapo Kwake.

41 Ine ndinangokhala apa, ndimayang'ana pompano mwa omvetsera. Ndipo ine ndikuwona a—mzanga wa ine, Akazi a Cox, ochokera kumusi mu Kentucky. Anali ndi khansa yaikulu pa nkhope yawo, masabata angapo apitawo, inali itawadya kwambiri kuzungulira diso lawo. Iwo amafa. Akazi a Wood, mzanga wabwino, anandiimbira ine foni, ndipo amalira, anati, "Ine ndikukhulupirira iyo idya diso la amayi kulichotsapo, mu masiku pang'ono." Adokotala anayamba kuligwiragwira ilo, ndi zinthu za mtundu winawake, ndipo analibalalitsa ilo. Ilo linali movuta kukonzeka. Ndinalowa mkati ndipo ndinakapereka pemphero lophweka, laling'ono, ndi chikhulupiriro chozikika, kuti izo zichitika. Ndipo ndi uyu wakhala apa usikuuno, wabwino mwangwiro ndipo wachira; wopanda ngakhale kadontho ka iyo katatsala, iyo yonse yachiritsidwa, pa nkhope yake. Wakhala pomwe pano kutsogolo kwathu. Ena azungulira, ali ndi chinthu chomwecho. Bwanji? Ndicho chifukwa chakuti Yesu Khristu anauka kwa akufa, ndipo Iye ali moyo.

42 Mmodzi yemwe uja amene amakhoza kukhudza wakhate, ndipo amati, "Ine nditero, iwe yeretsedwa," akhoza kukhudza khansa ndi kuti, "Ine nditha, khalani inu oyera," ngati Iye ali yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse.

43 Ndipo pamene Kleopa ndi iwo amayenda limodzi, okhumudwa, iwo anali ngati mu umodzi wa mmawa wa chisoni uja, akuwoneka ngati chirichonse chilakwa. Ndipo mwadzidzidzi, Winawake anatulukira, pamene Iye amabwera

kumbuyo kwawo, anayenda ndipo anadzapezana nawo iwo. Ndipo samadziwa kuti ameneyo anali Ambuye Yesu! Iye anali wamoyo, ndipo anthu ambiri amene ankamukonda Iye samadziwa zimenezo.

44 Ndipo ndicho chimodzimodzi monga mmene izo ziliri lero. Pali anthu ambiri lero amene amawakonda Ambuye, ndipo sakuzindikira. Inu mukhoza kuwauza iwo zokhudza izo, ndipo komabe iwo sangathe kuzindikira kuti Iye ali moyo kwa nthawi zonse, usikuuno, kuti Iye ali muno mu tchalitchi muno usikuuno, kuti Iye ali pakati pathu, ndipo izo zitero mpaka Iye adzabwera mu thupi, thupi logwirika. "Ine sindidzakuchokerani inu kapena kukusiyani inu."

45 Ndipo pamene iwo amapitirira, ndipo nayamba kuyankhula, akuyenda pa njira. Yesu, ine ndikufuna kuti inu muzindikire chinthu choyambirira chimene Yesu anachita, anapita molunjika ku Lemba. Iye anati, "Oh, opusa mu mtima, kodi ndi zovuta kwa inu kuti mukhulupirire chimene aneneri ananena?" Pakuti, Iye anali atangowafunsa iwo, "Chifukwa chiyani inu muli achisoni kwambiri?"

46 Ndipo iwo anati, "Kodi Iwe ndi mlendo? Kodi Iwe sukudziwa kuti Yesu wa ku Nazareti, Yemwe ife timamuganizira kuti Iye ndi Mesiya, Muomboli wa Israeli, kodi iwe sukudziwa kuti lino ndi tsiku lachitatu kuyambira pamene Iye anapachikidwa? Iye anali munthu wamphamvu, mu Mawu. Iye anali mneneri wamphamvu, chifukwa ndi zozizwitsa zambiri ndi zinthu, zimene Mulungu amachita kudzera mwa Iye. Ndipo lero ndi tsiku lachitatu; ndipo tsopano iwo amupha Iye, ndipo amuika Iye mmanda, ndipo Iye anali mmanda. Ndipo akazi ena anabwera kwa ife ndipo adzatiuza ife kuti Iye anali atauka kwa akufa. Ndipo ife tadziwa kuti zinangokhala nthano zopusa, kotero ife tiri pa njira yathu tikubwerera."

47 Ndiye apo ndi pamene Iye anayamba kutsegula Mawu. Oh, ine ndimawakonda Mawu Amuyaya a Mulungu! Iye anayamba kudutsa mu Malemba, kuyambira ndi Mose. Iye sanasiye kalikonse kosakakhudza, Iye anapita molunjika ku Mawu!

48 Munthu aliyense wotumidwa ndi Mulungu, ine sindikusamala kaya iye ndi ndani, iye adzakhala ndi Mawu a Mulungu. Ngati iye satero, iye si wantchito woona wa Mulungu.

49 Iye anapita molunjika ku Mawu. Ndipo Iye anawonetsera, mwa Mawu, kuti Khristu ankayenera kufa, kuukanso, ndi kulowa mu Ulemelero Wake. Tsopano, oh, momwe iwo ayenera kuti anayankhula!

50 Ine ndikanakonda ndikanakhala ndi maora pang'ono awo oyankhula ndi Iye (sichoncho inu?) pa njira. Inu mukuti, "Chabwino, M'bale Branham, ine ndithudi ndikanatero. Ndikukhumba ine ndikanatero." Chabwino, ife tikhoza kukhala

nazo izo pakali pano. Ndi Iyeyo akuyankhula ndi inu, mu mtima wanu. Zangokhala kuti inu simukuzindikira izo.

51 Tsopano zindikirani pamene Iye amayandikira mu mzinda, madzulo anali akubwera, Iye anatsogola ngati kuti Iye akufuna kuwadutsa iwo.

52 Iye akhoza kuchita zimenezo kwa inu, aponso. Iye akhoza kukupangani inu kuganiza kuti iye akudutsa kuti akupitirireni, koma Iye sakutero. Iye sakudutsani. Iye akungofuna kuti inu mumuitane Iye.

53 Ndipo iwo ananena kwa Iye, "Oh, tsikuli latha kale. Tsopano musapitirire, koma chonde lowani ndipo mukhale ndi ife." Inu mungomupatsa Iye kuitana kwa mtundu umenewo, mudzapeze chimene chiti chidzachitike. Anati, "Tsikuli latha kale tsopano, Inu mubwere ndipo mudzakhale ndi ife. Kukuyandikira kuda." Kenako Iye anapotoloka ndipo anakalowa mkati, pa kamalo kodyera, mogona alendo mwamung'ono.

Ku Ulaya iwo akadali nawobe iwo. Iwe umadya nkugona, ndipo zonse zimakhala kuti zalipiridwa mu bilu imodzi, hotelo yako.

54 Ndipo pamene Iye analowa mkati ndi iwo! Apa pali gawo lokongola. Tsiku lonselo, pamene iwo anali kuyankhula ndi Iye, Iye sananene konse chinthu chimodzi. Komabe, iwo anali atayendapo ndi Iye ndi kuyankhula naye Iye, nthawiina, koma iwo sanazindikire izo.

55 Ndani yemwe anakutetezani inu kuti musachite ngozi ija tsiku lina? Ndani yemwe anamuloleza mwana uja kuti akhale bwino? Ndani yemwe anakulipirirani bilu ya zogula zapanyumba ija? Anali Iyeyo, koma inu basi simunazindikire izo. Ndani yemwe anakupatsani inu thanzi kuti mubwere ku tchalitchi usikuuno? Ndi Iyeyo, koma inu simunazindikire izo. Oh, ngati ife titangochita monga iwo, kungomuitana Iye kuti alowe mkati!

56 Ndipo pamene Iye anadzalowa, anafika mkati, anatseka zitseko, ndiye Iye anachita chinachake chimene munthu aliyense sakanachita mwa njira imeneyo. Iye anali Mmodzi yekhayo amene akanatha kuchita zimenezo, pakuti iwo anakhala ndi Iye kupachikidwa Kwake kusanachitike. Ndipo Iye anatenga mkate umenewo, ndipo, basi monga mmene Iye ankachitira izo, iyo inali njira Yake Yokha yochitira izo. Ndipo maso awo anatseguka, ndipo iwo anadziwa kuti ameneyo akhoza kukhala Iye basi. Iye sanakhalitse ndi iwo nthawi yaitali. [M'bale Branham akukhwatchitsa chala chake—Mkonzi]. Iye anasowa pamaso pawo, mu mphindi chabe.

57 Ndipo ali pa njira yawo, iwo anabwerera molimba momwe iwo akanathera, opepukidwa poyenda, akungofuula chigonjetso, kukawauza iwo kuti, "Ambuye ndithudi awuka!" Iwo sanabwerere kukakangana za chipembedzo chawo.

Iwo sanabwerere kukalimbana zokhudza Izo. Koma iwo anangodziwa kuti Iye anali atauka kwa akufa!

58 Tsopano, mzanga, ngati Yesu Khristu, Mwana wa moyo wa Mulungu, zitatha zaka naintini handiredi zapitazo; ngati Baibulo liri lowona, Iye anati, "Ine ndiri wamoyo kwanthawi zonse"; Iye ali basi wamoyo muno, mchipinda chino usikuuno, monga Iye analiri tsiku la chiukitsiro Chake. Iye ali chomwecho mu thupi.

59 Ena a iwo anasonkhana pamodzi. Ndipo Iye anabwera kudzera mmakoma, anadzawonekera mkati momwe, kudzera pakati pawo, anati, "Apa, ndikhudzeni Ine. Taonani zipsyera Zanga mmanja Mwanga. Kodi mzimu umakhala ndi mnofu ndi mafupa ngati zimene Ine ndiri nazo?" Iye anati, "Ndipatseni Ine chinachake kuti ndidye." Ndipo iwo anamupatsa Iye nsomba ndi mkate. Ndipo Iye anaima pamenepo ndipo anadya izo, pamaso pawo, anati, "Mzimu sumadya monga mukundiwonera Ine ndikudya."

60 Kodi Iye ndi chiyani? Iye ndi wamkulu uja, Yehova Mulungu wamoyo amene ali pakati pathu usikuuno. Iye ali pakati pa paliponse pamene awiri kapena atatu asonkhana: "Ine ndidzakhala pakati pawo."

61 Ndipo tsopano apa pali chimene ine ndikuganiza. Ngati Khristu angabwere kwa omvetsera a anthu awa, pamene inu mukuchita thukuta, mukudikirira; ndipo atsimikizira, pa Isitara iyi, kuti Iye ali moyo, ndipo akuima mchipinda chino usikuuno; ndiye inu muli ndi ufulu womupempha Iye chirichonse chimene Iye anachifera, ndipo mukhulupirire kuti inu mulandira icho. Kodi inu mukukhulupirira zimenezo kukhala Choonadi? [Osonkhana akuti, "Ameni."—Mkonzi]. Ndithudi, izo ziri.

62 Tsopano, ine ndikhoza kuyankhula ndi inu motalika, koma Mawu amodzi ochokera kwa Khristu atanthauza mochuluka kuposa mawu onse amene ine ndingathe kuwayankhula; ndatopa ndipo mawu asasa, ndipo ndafooka monga momwe aliri mawu.

63 Ndiyeno chinthu china, mukuyankhula. Ndi zovuta, pakuti kuno ndi kwathu, kuti ndikhale ndi msonkhano wopambana ndi kuzodza kwa Mzimu monga choncho. Bwanji? Chifukwa kuno ndi kwathu. Yesu ananena kuti, "Mneneri, kwawo, dziko la kwawo, ngakhale mu dziko lakwawo lomwe." Izo ndi chinachake basi chimene chimachitika mwanjira imeneyo.

64 Iwo ananena kuti pamene Iye anapita Kwawo Komwe, iwo anati, "Kodi uyu si mwana wa mpalamatabwa? Kodi amayi Ake si, Maria, yemwe amakhala ndi ife? Kodi abale Ake onse samakhala kuno, ndi azilongo Ake? Kodi ife sitikuwadziwa iwo? Kodi Iye anachokera ku sukulu iti? Kodi Iye anaphunzira ku seminare yake iti? Kodi Iye ali ndi zipepala zotani?" Ndipo Iye sanadutse mu sukulu iliyonse kapena seminare iliyonse, kapena

zikalata zirizonse, koma Iye anachokera kwa Mulungu. Koma iwo samatha kuziwona izo. Iwo anati, "Kodi Iye nzeru zimenezi akuzitenga kuti?"

65 Ndipo pamene iwo anamuwona Iye akuzindikira malingaliro amenewo a anthu. Pamene Petro anabwera kwa Iye, Iye anati, "Dzina lako ndiwe Simoni. Dzina la abambo ako ndi Yonasi."

Izo zinawagwetsera iwo pansi! "Iye anawadziwa bwanji iwo?"

66 Afarisi anaima pambali, ndipo anati, "Iye ndi Belezebule. Iye ndi mfumu wa am'bwebwe. Iye ndi mdierekezi!"

67 Ndipo Yesu anati, "Inu mukunena zimenezo motsutsa Ine, Mwana wa munthu, izo zikhululukidwa kwa inu. Koma pamene Mzimu Woyera udzabwera ndipo nkudzachita chinthu chomwe chomwecho, ndipo inu nkudzayankhula mawu amodzi motsutsana ndi Iwo, izo sizidzakhululukidwa kwa inu, mu dziko lino kapena dziko limene liri nkudza." Chotero, icho ndi chinthu chowopsya. Chotero Iye anadziwa bwanji? Nchifukwa chiyani Iye ananena zimenezo? Iye ankadziwa kuti zizindikiro zimenezo zikanadzasiya kufikira tsiku lotsiriza lino.

68 Ndipo masiku otsiriza ano, Iye sakanadzakhala wolungama, kuti atsanulire mkwiyo Wake pa anthu olungama. Iwo ali . . . Ife tayesedwa pa muyezo, ndipo tapezeka operewera. Zonse zimene ife timaziganizira ndi nthawi zazikulu, maprogramu apa wailesi, osasefedwa, Elvis Presley, Arthur Godfrey, nthabwala zoipa zakale, odziwika a pa wailesi ndi pa televizioni. Ife timakhala kunyumba Lachitatu usiku, kujomba msonkhano wa pemphero, kuti tiziwonera zovunda ngati zimenezo, ndi kumadzitchula tokha Akhristu?

69 Ndiye pamene Mulungu atsanulira pansi Mzimu Wake, ndi kuwonetsera zizindikiro za chiukitsiro Chake, ife timazitsutsa Izo ndipo timatembenukira kutali. Ndipo limenelo ndi tchimo losakhululukidwa, kuchita zimenezo. Yesu anati, "Kuyankhula mawu amodzi motsutsa Izo, izo sizidzakhululukidwa konse, mu dziko lino kapena dziko limene liri nkudza." Chotero Mzimu umenewo ukuyenera kubwera mmasiku otsiriza ano, kudzatsimikizira kuti Mawu a Mulungu amenewo ndi owona.

70 Ndipo ine ndikuti, pansi pa ulamuliro wa Mawu a Mulungu, ndi kumverera kwa moyo wanga womwe: Mzimu Woyera (Mzimu) womwewo uli pomwe pano tsopano pakati pa anthu awa. Tsopano, ine ndinanena kuti Iye wauka kwa akufa. Ine ndinanena kuti Iye ali moyo, wamoyo kwa nthawizonse. Ine ndinadzinenera kuti Iye ali yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse; yemweyo mu mfundo, yemweyo mu Mphamvu; yemweyo mu chirichonse, zonse kupatula thupi Lake logwirika limene likukhala ku dzanja lamanja la Mulungu ndi Ulamuliro, mu Ulemelero. Koma Mzimu Woyera uli pano, ukugwira ntchito, ukuyendayenda, ukuchitachita, ukuchita ndendende basi monga

Yesu Khristu ankachitira, pakuti ndicho chitsimikiziro cha chiukitsiro Chake. Ndi ora lokongola bwanji! Tsopano ine ndikuganiza inu mwaona pamene ine ndikuima.

71 Tsopano, osati kokha ndi apang'ono awa, a pafupifupi anthu handiredi, kapena anthu thuu handiredi muno mu—mchipinda chaching'ono chino, tadzazana muno usikuuno, koma ine ndapangapo neno limenelo pamaso pa masauzande kuchulukitsa masauzande, ndi mahandiredi a masauzande. Ndinagwira Baibulo dzanja limodzi, ndi Korani linali, ndikuti, "limodzi ndi lolondola, ndipo linali ndi labodza." Ndi kumubetchera wansembe aliyense wa Chimuhamadi kuti abwere ndi kudzatsimikizira; kapena wina aliyense, Buddha, kapena chirichonse chimene iye angakhale, ndinatsutsa Korani, ndi kutsutsa chipembedzo chawo. Koma aliyense anangokhala chete.

72 Koma, abale, chifukwa chimene ine ndimachitira zimenezo, chifukwa ine ndikudziwa Muomboli wanga ali moyo! Ndipo Iye ali Choonadi. Yesu Khristu ali moyo. Iye ali muno!

73 Tsopano mulibe kanthu mwa inemwini kamene ine ndingathe kuchita, iyo ndi mphatso ya Mulungu. "Inu mumachita motani izo?" Ndi kungodzipereka iwemwini.

74 Mchipinda momwemuno tsopano muli ambiri, Angelo ambiri. Inu mukuti, "Kodi limenelo ndi Lemba?" Limenelo ndi Baibulo. Ndiloleni ine ndikuwonetseni inu. Ndi Akhristu angati ali muno, kwezani dzanja lanu? Chabwino, inu mukhoza kuwatsitsa iwo pansi. Baibulo linanena kuti, "Angelo a Mulungu amazinga iwo amene amamuwopa Iye." Ndiye, pali Angelo pano!

75 Ndiye Khristu anati, "Paliponse pamene awiri kapena atatu asonkhana mu Dzina Langa, Ine ndidzakhala pakati pawo." Ndiye, Iye ali pano! Chinthu chokhacho chmene chiri, inu simungathe kumuwona Iye, koma mwa chikhulupiriro ife tikukhulupirira izo.

76 Ine ndikhoza kutsimikizira kwa inu kuti wailesi ikudutsa muno, aponso, maliwu. Ine ndikhoza kutsimikizira kwa inu kuti zithunzi zikubwera kudzadutsa muno. Izo sizingadutse pa chubu *ichi* apa; izo sizingadutse pa *ichi*, galasi ili, kapena choyankhulirapo ichi; komanso izo sizingabwere pa chidutswa *ichi* cha nsalu, chifukwa icho sichinapangidwe mwanjira imeneyo. Koma pali chidutswa cha chinthu chimene chingawonetse chithunzi chimenecho.

77 Ndipo Mulungu anawaika ena mu Mpingo, poyamba atumwi, kenako aneneri, aphunzitsi, avangeri, ndi azibusa, onsewo kwa ungwiro wa Mpingo. Ife tingamukane bwanji wina, ndi kuti winayo sali choncho? Mulungu amachita izo, Iyemwini. Si kalikonse mu dziko koma kungodzipereka wekha kwa Mzimu Woyera. Ndipo Mzimu Woyera umapitiriza kuyambira

pamenepo, ndipo iwe sumadziwa chimene iwe ukuchita. Ndi ntchito ya payekha ya Mzimu Woyera.

78 Tsopano, abwenzi, mzinda wa kwathu. Ndipo ine ndikufuna ndinene ichi tsopano, ndisanatseke chitsitsimutso ichi. Limodzi la masiku awa sipadzakhala ngakhale phulusa lidzatsale mu Jeffersonville, sipadzatsala mmodzi mu Charlestown, sipadzatsala mmodzi mu Louisville. Dziko ili lakhwima kuti liweruzidwe. Iwo ali ndi bomba la haidrojini tsopano limene Russia akhoza kuwombera kuchokera ku Moscow, kudzaliteretsa ilo pa Fourth Street, ndikuzula makina aliwonse opangira mkaka waufa awa kuno, ndi kuwamiza iwo mapazi sevente-faivi pansi pa dothi, ndi bomba limodzi. Bomba limodzi; kuzungulira mamailosi fifitini, izo nkupita mapazi handiredi fifite pansi pa nthaka. Dzanja liri pa chokhethemulira. Koloko ikuyenda mopita. Ndi mochedwa kuposa momwe inu mukuganizira. Chifukwa chiyani mukudikirira kufikira nthawi imeneyo?

79 Kumbukirani, "Msasa wapansi pano ukapasuka, ife tiri nawo wina ukudikirira." Musachite mantha ndi mabomba a haidirojini kapena chinthu china. Bola ngati inu muli ndi Khristu mu mtima mwanu, ndi powusirapo bomba pa pamwamba pamene ine ndikupadziwa. Ipo ndi popangidwa ndi nthenga; pansi pa mapiko Ake, inu mwakhalapo. Chotero musadandaule zokhudza zinthu zimenezo, ngati ndinu Mkhristu.

80 Koma ngati sindinu Mkhristu, inu ndithudi mwaima pa malo owopsya. Inu simukudziwa ndi miniti iti imene mtima wanu utasiye kugunda. Baibulo linati amuna adzafa mmasiku otsiriza, ndi vuto la mtima, "Mitima ya amuna ikulephera, ndi mantha, nthawi zowawitsa, mavuto pakati pa mafuko." Taonani kuchuluka kwake, kuchulukitsa ka teni amuna ambiri akufa, kuyerekeza ndi akazi; Baibulo silinanene konse kuti mitima ya akazi idzakhala ikulephera, Ilo linati, "Mitima ya amuna idzakhala ikulephera." Ndizo mwamtheradi, mwangwiro.

81 Tsiku lina mu Oakland, mkazanga ndi ine tinali kumeneko mu San Francisco, chivomerezi champhamvu chija chinagwedeza. Ndipo dziko linayamba kusanza ndi chidikhodikho pamenepo, kufikira zinyumba zinagwedera, ndipo zimuni zinagwa. Mipira yaikulu ya mpweya inapita mmwamba monga *choncho*, ndi utsi mwa iyo, kapena mwaye, chirichonse chimene icho chinali, kuchoka mmalo amenewo. Ndipo anthu anathamangira mmisewu, akufuula. Ine ndinaganiza, "Chidzakhala chiyani pamene Ambuye ati adzawonekere kwenikweni?" Momwera mowa, kumapitirira, kumaika mowa wawo, kubwezeretsa pa mashelofu, ndi kumagulitsa iwo. Anthu kumabwera kudzagula iwo. Munthuyo sibwenzi akugulitsa ngati pakanati pasakhale amene akudzagula iwo. Zoona zimenezo.

82 Ndi, ife ndi amene tiri olakwa. Ndiloleni ine ndikuuzeni inu, m'bale. Ine ndi wa Chimerika, ndipo ine ndimalikonda dziko langa. Koma fuko lakale ili layesedwa pa sikelo, ndipo lapezedwa loperewera. Ilo likumira, motsimikiza basi monga ine ndiri mtumiki kuseri kwa nsanja iyi usikuuno. Tsopano ine ndikunena zimenezo kuti ndipeze kukonderedwa ndi Mulungu. Ine ndikunena zimenezo chifukwa Mulungu waziika izo pa mtima wanga kuti ndinene izo. Ndipo chinthu chopambana kuti inu muchite ndi kukonzekera Kubwera kwa Ambuye.

83 Tsopano mukhulupirireni Iye, mukhale ndi chikhulupiriro mwa Iye. Tsopano, mawu onse amene Ine ndinganene, Ine ndikunenanso, sakanatanthauza kanthu kamodzi kwa chimene Yesu akanayankhula. Koma kodi inu mukuzindikira pamene ine ndaima, ndi gulu ili la anthu awa usikuuno? Ine mwina ndasokoneza, ndatanthauzira molakwika chinachake, kapena ndanena Choonadi. Tsopano ngati Yesu Khristu anauka kwa akufa, ndipo, analonjeza, zinthu zomwezo Iye anazichita ife tidzazichitanso. Ndipo ine ndadzinenera, kuyambira ndiri khanda laling'ono mnyamata . . .

84 Ine sindinali usinkhu wa miyezi eyitini, ine ndikuganiza, koma osapitirira zaka ziwiri, mulimonse, pamene ine ndinawona masomphenya anga oyambirira. Izo, zakhala, moyo wanga wonse. Anthu muno mu kachisi, akudziwa zimenezo. Nthawi zonse zimene ine ndakhala ndiri pano, palibe nthawi imodzi imene izo zinayamba zalepherapo. Ndipo izo sizidzalephera konse, chifukwa izo ndi Mulungu. Kuzungulira dziko izo zapita, chitsitsimutso chachikulu chayaka. Ndipo tsopano, mwa chisomo cha Mulungu, ine ndiri mu miyoyo mamilioni awiri anga achiwiri, mu msonkhano wanga kumene, kupindulira kwa Ambuye Yesu. Millioni yachiwiri, uko nkulondola. Ndipo tangoganizani za mamilioni ena amene atuluka, Oral Roberts, moto wonse uja umene wayatsidwa kuchokera kwa chinthucho, ndipo umapitirirabe, masauzande kuchulukitsa masauzande, kufikira kuti kuzungulira dziko pakhala chitsitsimutso chimodzi chachikulu chopambana cha Mphamvu ya Mulungu, chikuyenda. Ndipo mdierekezi akumasula mitundu yonse ya zinthu zabodza, kuti atsutse Iyo. Koma enieni, Mawu owona a Mulungu apita molunjika mpaka kumapeto. Iwo sadzalephera konse! "Ine Ambuye ndawabzala iwo. Ine ndiziwathirira iwo usana ndi usiku, kuwopa kuti wina angawakhwatule iwo kuchoka mdzanja Langa."

85 Tsopano, usikuuno, ine ndinanena kuti Khristu anauka kwa akufa. Iye ali yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse. Tsopano, Ambuye akudalitseni inu. Ngati Iye ati achite zimenezo, ndiye ndinu . . . Ngati inu mukukhulupirira zimenezo, Mulungu akudalitseni inu. Mpempheni Iye, ndiye, pamene Iye ati abwere powonekera. Ngati Khristu ati awonekere pano pa nsanja ino! Pano pali chovuta. Ngati Yesu Khristu, Mwana wa

Mulungu, ati awonekere pomwe pano pa nsanja, ndi kudzachita zinthu zomwezo zimene Iye anachita pamene Iye anali kuno pa dziko lapansi, kodi inu mumukhulupirira Iye? [Osonkhana akuti, "Ameni."—Mkonzi].

86 Yang'anani pa Iye, ali pa njira yopita ku Emmau, mmene anyamata amenewo, ananyemera . . . Pamene Iye ankanyema mkate umenewo, Iye anachita chinachake pamenepo chimene munthu wina aliyense sakanachita. Icho chinali chinachake chimene Khristu yekha akanachichita. Ndipo iwo anachizindikira icho.

87 Tsopano ngati Iye angadzachite chinthu chomwecho pano, chimene Khristu yekha angathe kuchichita; osati chinthu china chabodza, koma chinthu chomwe chomwecho chimene Iye anachichita; ndiye inu mumukhulupirire Iye, mumulandire Iye, mukhale ndi chikhulupiriro mwa Iye, mumukonde Iye, mumutumikire Iye.

88 Mundilore ine ndikuuzeni inu, musati mungojowina mpingo tsopano. Zimenezo sizigwira ntchito. Inu mukuyenera kubadwanso mwatsopano. Osati ntchito ina yongotengeka; osati chaching'ono chinachake chimene iwe unanena, "Chabwino, ine ndinafuula. Ine ndinayankhula ndi malirime. Ine ndinachita *ichi*, *icho* kapena *chinacho*." Pamene kwenikweni pansi mu mtima mwanu, Chinachake chimabwera kudzakusinthani inu, ndipo inu mumadzakhala cholengedwa chatsopano mwa Khristu Yesu; inu munamulandira Munthuyo, Khristu Yesu; pamene zinthu zakale zifa, ndipo zinthu zatsopano zibadwa kenanso; inu mumakonza zinthu, zimene inu munachita molakwitsa; inu mumawakonda adani anu, inu mumawapempherera iwo amene amangokugwiritsani inu ntchito mwa mnyozo; pamenepo ndi pamene inu mumakhala Mkhristu. Mtengo umadziwika ndi zipatso zimene iwo ukubala.

89 Ambuye akudalitseni inu tsopano, pamene ife tikuweremitsa mitu yathu. Ine ndimufunsa mlongo kuti apite pa limba, mwapang'onopang'ono aziyimba *"Nsing'anga wamkulu tsopano wayandikira, Yesu wachisoni."* Ndipo inu amene muli panja, tsopano, amene muli ndi makadi a pemphero, musunthire pafupi ndi chitseko, ife tiyamba mu mphindi chabe. Tiyeni tipemphere.

90 Atate athu Akumwamba Odala. Oh, mawu anga osauka, miyezi inai yoyankhula, ine ndangokhala wotopa kwambiri mu mawu anga. Koma ine ndikupemphera kuti Inu mundithandize ine basi tsopano. Apa pakhala mphondero ina pa Branham Tabernacle. Apa padzakhala mboni ina iti idzawuke mmasiku otsiriza, pa Tsiku la Chiweruzo. Ambiri aimirira mkati ndi panja, usikuuno, ambiri a iwo akudabwa, ambiri akuganiza, "Kodi izi ndi zoona, kapena izo si zoona?"

91 O Atate a Muyaya ndi Wodala, ife tikupemphera kuti Inu tsopano muwonetsere chikondi Chanu kwa ife, powonekera

pano ndi kuwapangitsa Mawu Anu kukhala owona. Ine ndayankhula za Mawu Anu; monga Inu munachitira, Inumwini, kwa Kleopa ndi mzake, waku Emmau. Ndipo pa njira yathu, Ambuye, pamene ife tikuyenda, Inu muyankhule nafe ife kudzera mu Mawu Anu. Ndipo tsopano mubwere pakati pathu! O Khristu Wamkulu, mubwere pakati pathu, mudzatsimikizire Mawu Anu kukhala owona, ndipo muwonetsere Umunthu Wanu pano usikuuno. Pamene, ife zolengedwa zosauka zosayenera tikuvomereza kuti ife ndi ochimwa ndipo osayenera zinthu izi, koma ife tikukhulupirira izo, Ambuye. Ndipo mwa chisomo ife tikulandira izo, kupyolera chikhulupiriro, kuti ife tinapulumutsidwa, ndipo ana Anu. Tidalitseni ife tsopano, Ambuye.

92 Ine ndikuwadziwa Mawu Anu ndi owona, pamene Inu munanena zokhudza "mneneri kwawo, pakati pa anthu ake omwe." Koma, Ambuye, ine ndikupemphera, basi kwa usikuuno, kuti Inu mudzangoyang'ana pansi kwa anthu, ndipo mudzadziwonetsere Nokha kamodzi kokha pano mu mzinda uno, kupyolera mu kusuntha kwa Mzimu Woyera. O Mulungu Wamuyaya, tidalitseni ife tsopano pamene ife tikudikirira pa Inu. Ndipo muchite zinthu zimene Inu munazichita kupachikidwa Kwanu kusanachitike, ndipo Jeffersonville akhala wopanda kanthu kamodzi kodandaula. Koma, ife tikudziwa kuti iwo adzakhala opanda chowiringula pa Tsiku limenero, kuti Inu mwadziwonetsera Nokha. Mu Dzina la Yesu, ine ndikupemphera. Ameni.

93 [Malo opanda kanthu pa tepi—Mkonzi.]. . .si chimene iye akufuna kuti ine ndipempherere. Ayi, iyo si khansa, pakuti iye anachiritsidwa kwa iyo. Koma iye akufuna kuti ine ndipempherere vuto la nsana limene iye ali nalo. Uko nkulondola. Ndi vuto mu nsana wake. Nkulondola uko? Tsopano kodi inu mukukhulupirira kuti Iye anauka kwa akufa? Tsopano penyani. Ngati ine ndingayankhule ndi iye motalikirapo pang'ono, mwinamwake china chakenso chikhoza kuyankhulidwa. Ine sindikudziwa. Tsopano, ine ndinalibe lingaliro kuti vuto lanu ndi chiyani. Ine sindikudziwa tsopano chimene ilo linali. Mukuona? Koma zojambulira zajambula izo, inu mukhoza kukapeza chimene Iye ananena.

94 Tiyeni tiyankhule miniti chabe motalikirapo, ndipo tiwone ngati Iye angandiuze ine chinachakenso. Ine ndikuwona mkazi amene akuwoneka ngati chinachake mwa dongosolo. . .Ndi mkazi wina, ndipo iye akumupempherera iye. Ndipo iye ali mu mtundu wina wa kwa amisala kapena chipatala, kokhala ngati. . .Ndi malo amisala. [Mlongo akuti, "Inde."—Mkonzi]. Ndi Madison, Indiana. ["Zoona zimenezo."] Ndi—ndi a—ndi a—mlongo amene inu mukumufunira pemphero, ndi kwa amisala. Ndipo ngati inu mungakhulupirire ndi mtima wanu wonse, ndi zonse zimene ziri mkati mwa inu, Mulungu akuwombolani ndipo

achiritsa nsana wanu ndi kukupangani inu kukhala bwino. Inu mukukhulupirira zimenezo tsopano? Chabwino, bwerani apa.

95 Wokondedwa Atate Akumwamba, ife tikupemphera kuti mu Dzina la Yesu Khristu, kuti Inu mumuchize mkazi uyu, ndipo mumupange iye akhala bwino. Ndipo mupereke dalitso ili kwa iye. Ndipo ine ndikupemphera kuti zifundo za Mulungu zikakhale pa iye, ndipo mukamuchiritse iye, ndipo mukadzitengere ulemelero kwa Inumwini. Ine ndikupemphera mu Dzina la Yesu Khristu. Ameni.

96 Ine ndikhoza kunena izi. Pali kunjenjemera kukuchokera kumeneko, kuchokera mmbuyo *kuno*. Mphindi chabe, mungoima pamenepo miniti chabe. Ine ndinazindikira Kuwala kuja kwakuchokerani inu. Pali ochuluka kwambiri, mwaunjikana kwambiri mondizungulira ine pano. Aliyense akukoka. Koma ine ndikukuwona Iko kukusunthira kwa inu. Ndi winawake amene . . . Inu muli—mukhala ndi opareshoni yachikazi imene ikubwera. Uko nkulondola. Ine ndinawawona anthu awiri kapena atatu akuwonekera, ndipo Kuwala kunathawira kumbuyo kumeneko ndi kukamugunda munthu uyo waima kumbuyo uko. Ndi iwowo akupempherera izo. Mukuona? Uko nkulondola. Ndipo inu muli, ndi chochitika cha dona amene ali ndi opareshoni yachikazi. Uko nkulondola. Tsopano pitani ndipo mukalandire machiritso anu, ndipo Ambuye Mulungu akupangani inu kukhala bwino. Ameni.

97 Kodi inu mungabwere? Dona, kodi inu mukukhulupirira pa Ambuye Yesu? [Mlongo akuti, "Inde, bwana."—Mkonzi]. Kodi inu mukukhulupirira kuti Iye anawuka kwa akufa? Tsopano, kukudziwani inu, ine sindikutero. Ine mwinamwake ndinakuwonanipo inu ngati muli wochokera kozungulira kuno. Ine sindikudziwa. Anthu amabwera ndikupita, ine sindimakhala khala ku kachisi kuno nthawi yokwanira kuti ndikudziweni. Koma, inu, inu ndi wochokera mu mzindawu? ["Inde."] Inu ndi wochokera mu mzindawu. Chabwino, ndiye, koma ine sindikukudziwani inu. Koma Khristu amakudziwani inu. Koma ngati Iye angawulule kwa ine, nditaima pano, chimene inu mwadzera pano, kodi inu mukhulupirira izo ndi kuvomereza izo? Ndipo inu mukudziwa ine sindikudziwa chimene inu mwabwerera pano, ndiribe lingaliro ayi. Chinthu chokhacho, inu mwina mukhoza kukhala kuti munandiwona ine mozungulira mzindawu, kapena chinachake, kapena, kapena chinachake. Ine sindikudziwa. Izo ziri kwa Mulungu kuti—kuti adziwe zimenezo.

98 Kumbuyo komwe uko, inu mukufuna kuthana ndi vuto la mmimba limene inu mwakhala muli nalo? Kodi inu mukukhulupirira Ambuye Yesu akhoza kukupangani inu kukhala wabwino bwino? Ngati mukukhulupirira izo, inu mukhoza kukhala nazo izo.

99 Wina ali ndi kuchuluka kwa magazi koyipa, wakhala kumbuyo uko, ine ndikuwawona iwo akutenga. Kodi inu mukukhulupirira kuti Ambuye akupangani inu kukhala bwino bwino? Chabwino. Kodi inu mukukhulupirira ndi mtima wanu wonse? Ndiye inu mukhoza kukhala ndi machiritso anu, Mulungu wakuchizani inu pomwepo. Inu munamukhudza Iye. Inu simunandikhudze ine, inu muli mapazi sarte kutali ndi ine. Ameni.

100 Tsopano kodi inu mukukhulupirira kuti Iye anawuka kwa akufa? Tangoyang'anani, ndipo mukhale moyo, tsopano pamene mzere ukusuntha. Oh, kodi izo ndi zovuta kwambiri kuno ku Jeffersonville! Mukuona? Ndipo unyinji ngati uwu kungokuzungulira iwe, aliyense! Yesu anamutenga munthu pa dzanja, ndipo anamutsogolera iye kutuluka mu tauni, nthawi ina.

101 Tsopano tayang'anani mbali iyi, mlongo, mphindi chabe. Mukukhulupirira kuti Ambuye Yesu ali pano kuti akuthandizeni inu. Inu mukuvutika ndi vuto limene liri mu thumbo, ndipo adokotala akupimani inu. [Mlongo akuti, "Inde."—Mkonzi]. Ndipo iye anakuuzani inu kuti zinali "zotupa mmimba." Ine ndikuwona inunso mukuyesera kuyenda kudutsa nyumba, ndipo inu mukuyenda pang'ono pang'ono kwenikweni. Inu muli ndi nyamakazi. ["Zoona zimenezo."] Ndizo PAKUTI ATERO AMBUYE. Adokotala ananena kuti inu mukuyenera kupangidwa opareshoni. Ndizo ndendende kulondola. Ndipo ine ndikumuwona iye akusaina ka khadi kakang'ono pamenepo pa ofesi yake: Rebekah Baker. ["Inde, bwana."] 509 Graham Street. ["Zoona zimenezo."] Ndiko kulondola ndendende. Umo ndi mu ofesi mwake, pa zolembedwa. Uko nkulondola. Kodi inu mukukhulupirira? ["Inde, bwana."] Ndiye inu mukhoza kukhala nawo machiritso anu. Mu, Dzina la Ambuye Yesu Khristu, mulole mkazi uyu alandire machiritso ake. Ameni. Mulungu akudalitseni inu, dona. Pitani, mukukhulupirira tsopano. Mukhale ndi chikhulupiriro mwa Mulungu.

Ngati inu mutangozindikira Kukhalapo kwa Ambuye!

102 Tsopano dona amene waima apa, kuti inu mukhoza... Ine sindikukudziwani inu, monga momwe ine ndikudziwira. Inu simukundidziwa ine, ndipo ine sindikukudziwani inu. Nkulondola uko? Chabwino. Ndiye inu ndi winawake amene samandidziwa ine, ndipo ine sindikuwadziwa iwo. Ndipo ine sindimamudziwa dona winayo. Koma dona uyu ndi mlendo kwathunthu, monga momwe ine ndikudziwira. Ngati izo ziri zoona, kwezani mmwamba dzanja lanu, dona. Nthawi yathu yoyamba, yokumana konse mmoyo.

103 Apa pali mkazi ndi mwamuna. Basi chithunzi chokongola cha Yohane Woyera 4, pamene mkazi ndi Mwamuna anakumana; ndipo mkaziyo anali Msamariya, Yesu anali Myuda. Ndipo iwo

anayamba kuyankhulana wina ndi mzake, ndipo Yesu anawulula zinsinsi za mu mtima wake ndipo anamudziwitsa iye pamene panali vuto. Tsopano, ngati Iye ali Yesu yemweyo lero, Iye akhoza kuchita ntchito yomweyo lero.

104 Ngati mkazi uyu angakwezere dzanja lake kwa Mulungu, osati kulumbira (chifukwa, ife sitimakhulupirira mu kuchita zimenezo), wangokweza dzanja lake mmwamba modzipereka, ndi langa, kuti ife sitinayambe takumanapo wina ndi mzake, ndipo sitikudziwa kalikonse ka wina ndi mzake. Kodi inu mungakweze dzanja lanu mmwamba, dona? Ndi zimenezotu. Iye sanayambe wandiwonapo ine, kapena ine sindinayambe ndamuwonapo iye, ndipo iye ndi mlendo kwathunthu. Tsopano ngati pali . . .

105 Kukhalapo kwa Ambuye Yesu kuli pano. Ngati mkaziyu akudwala, ine sindingathe kumuchiza iye. Iye wachiritsidwa kale; Khristu anamuchiritsa iye pamene Iye ankamufera iye. Kodi inu mukukhulupirira zimenezo? Koma ngati Iye akanakhala kuti akuima pano tsopano, ndipo—ndipo pamene ine ndaimapa, ndipo Iye akanatha, akanawulula kwa iye, kapena akanachita chinachake kuti chibweretse chikhulupiriro chake kuti tikumane! Tsopano, iye mwina waima pano chifukwa cha vuto la chuma. Iye mwina waima pano chifukwa cha vuto lapanyumba. Iye mwina waima pano, akufa ndi khansa. Iye mwina waima pano ndi TB. Ine sindikudziwa. Ine sindingathe kukuuzani inu.

106 Ndipo tsopano ngati inu mukufuna kuti mudziike inueni mu malo anga, bwerani pano ndipo mudzatenge malo anga. Ndinu olandiridwa. [M'bale Branham waimikira—Mkonzi]. Ndithudi. Ngakhale inenso sindikudziwa, ngakhale ine sindingachite izo. Koma Mulungu wa Kumwamba akudziwa. Kodi inu mukumvetsa tsopano? [Osonkhana akuti, "Ameni."]

107 Ndipo ngati Khristu angachite chinthu chomwecho pano, mu Choonadi chosalephera, ngati Iye wauka kwa akufa, ndipo anatsimikizira kuti Iye ali Yesu yemweyo amene anayankhula ndi mkazi pa chitsime, ndi angati muno akuti, "Ine ndimulandira Iye pompano ngati Mchiritsi wanga, kapena chirichonse ine ndikuchisowa"? Kwezani dzanja lanu, ndikuti, "Ine ndimulandira Iye ngati Iye atachite zimenezo."

108 Mkazi amene wakweza manja ake mmwamba, ife sitinakumanepo. Ambuye apereke icho, ndi pemphero langa. Tsopano donayo akuwoneka kuti akuchoka kwa ine; ngati omvetsera angathe kumvetsera mawu anga. Ine ndikumuwona winawake waimirira. Si za iyeyo, zochuluka kwambiri. Iye akumupempherera winawake, ndipo uyo ndi dona wachikulire. Iwo ndi amayi ake, amene akuwapempherera. Izo nzoona. Iye ali vuto la mtima pang'ono, mtima wawung'onowo ukunjenjemera, mokhala ngati. Iye akumalephera kugona usiku. Kodi si

kulondola uko? Kwezani dzanja lanu ngati izo ziri zoona. Ndipo dona ameneyo si wochokera mu dziko lino. Dona ameneyo akuchokera kutali ndi kuno. Dona ameneyo akuchokera ku Georgia. Ndizo ndendende kulondola. Ndipo ndinu wochokera ku Georgia. Ndipo inu mukufuna pemphero chifukwa cha diso lanu, inunso. Inu mukuchita khungu mu maso anu. Ndipo izo nzoona. Kodi inu mukukhulupirira kuti Mulungu akupangani inu kuti mukhale bwino? Ngati izo nzoona, kwezani mmwamba dzanja lanu. Chabwino.

109 Tsopano kodi inu mukukhulupirira? [Osonkhana akuti, "Ameni."—Mkonzi]. Tsopano mukhale ndi chikhulupiriro mwa Mulungu. Pamene ine ndikumupempherera iye, inu muzidzipempherera nokha kunja uko, ndipo mukhulupirire Mulungu. Iye ali pano, wopezekaponseponse.

Bwerani kuno, mlongo.

110 Mpulumutsi wodala, ine ndikupemphera kuti, mu Dzina la Khristu, kuti Inu mukapereke kwa mkazi uyu chokhumba chake. Mulole Mphamvu ya Mulungu Wamphamvuzonse ikhale pa iye, ndipo mulole iye achiritsidwe ndipo alandire chirichonse chimene iye wachipempha. Ine ndikupemphera mdalitso uwu mu Dzina la Yesu. Ameni.

111 Tsopano zipitani, mukusangalala, ndi wokondwa. Ndipo mukhulupirire, mlongo, ndipo mukakhale bwino. Chabwino.

112 Ine sindiri wotsimikiza, koma ine ndikukhulupirira ine ndikumudziwa mkazi uyu. Ine ndikukhulupirira inu mukuchokera ku Georgetown, chifukwa ndine . . . Kodi sindinu wachibale wa M'bale Arganbright? Ndithudi, tsopano kuzodza uku, ndi kosiyana. Inu mukuzindikira kuti pali kusiyana tsopano. Pamene ine ndiyankhula ndi inu kwinakwake; izo ndi zosiyana tsopano. Inu mwamverera kumverera kwabwino kwenikweni, chomwecho. Ndi Mzimu Woyera. Inu simuli pano chifukwa cha inueni. Inu muli pano chifukwa cha wina wakenso, ndipo ameneyo ndi mtsikana wamng'ono wapafupi zaka foro kapena faivi zakubadwa. Iye ali ndi vuto la impyso, ndipo iye amakhala kumpoto kwa Indiana. Izo nzoona. Icho chimene inu muli nacho mdzanja lanu, muchitumize icho kwa iye, ndipo iye achiritsidwa. Mukhulupirire ndi mtima wanu wonse tsopano, ndipo mulandire chimene inu mwachipempha, mu Dzina la Khristu.

"Ngati inu mungakhulupirire, zinthu zonse ndi zotheka!"

113 Apa pali dona yemwe ali mlendo kwa ine. Ine sindikukudziwani inu, sindinayambe ndakuwonanipo inu mmoyo wanga. Ife ndi alendo kwa wina ndi mzake, zaka zambiri kutalikana; mwinamwake zambiri, tinabadwa mamailosi ambiri motalikana. Ine sindikukudziwani inu, sindinayambe ndakuwonanipo inu. Koma Yesu Khristu amakudziwani inu.

114 Chinachake chachitika mwa omvetsera; munthu anawonekera pafupi ndi ine. Iye wakhala apa, pomwe pano, mchombo wotupa. Kodi inu mukukhulupirira, bwana? [M'bale akuti, "Inde!"—Mkonzi]. Ndiye Khristu akuchizani inu ndipo akupangani inu kukhala bwino! Ameni.

115 Iyo ndi njira yake yochitira izo, mukhulupirire! Kodi iye anakhudza chiyani? Ine sindinamuwonepo munthuyo; koma iye anachiritsidwa pomwe apo. Iye anawakhudza Ambuye Yesu Yemwe ali pano. Chotsani kusakhulupirira kumeneko kwa inu! Muiwale zoti ine ndi William Branham. Muyang'ane pa Yesu Khristu, Iye ndi Amene ali pano. Ine ndikubetchera chikhulupiriro chanu, mu Dzina la Khristu, kuti mukaiwale za ine; ndipo mukhulupirire kuti uyu ndi Yesu Khristu pano, ndipo muwone chimene chiti chichitike. Ine sindikusamala pamene inu muli mu mchipindachi.

116 Tsopano apa pali mkazi wachichepere. Ine sindinamuwonepo iye. Iye ndi wamkulu kuposa ine. Iye, ine sindikudziwa yemwe iye ali, kumene iye akuchokera, palibe chokhudza iye. Ine ndi mlendo wangwiro kwa iye. Koma Khristu akumudziwa iye.

117 Ngati Iye angawulule kwa ine chimene inu mwabwerera pano, kodi inu mulandira icho ndipo mukhulupirira icho? [Mlongo akuti, "Ndithudi."—Mkonzi]. Inu munali ndi kumverera kwachirendo maminiti pang'ono apitawo, pamene ine ndinayankhula chinachake, sichoncho inu? Iye anali mchemwali wanu ["Inde."] amene ali kwa amisala ku Madison, Indiana. ["Ndiko kulondola."] Kulondola kumeneko. Kwa, mkazi wina amaima apa, ndipo inu munali kuima pamenepo mukuyang'ana molunjika mbali iyi. Ndipo masomphenya, inu mumakhulupirira pamene inu mumabwera kuno. ["Ndithudi."] Ndizo ndendende kulondola. Ndicho chimene chachita izo. Ndipo chifukwa chimene inu mwadzera pano usikuuno, ndi chifukwa chakuti muli ndi vuto la mtima. Inu mwangokhala kumene ndi nthenda ya mtima. Ndizo ndendende kulondola. ["Zoona zimenezo."] Ndipo ine ndikuwona tsopano, pamene ine ndikuwona mmasomphenya, dziko logudubuka ilo. Inu mukuchokera kwinakwake kuno kummwera kwa Indiana. Ndinu wochokera kufupi ndi Corydon, uko ndi kumene inu mwachokera. Bwererani kwanu, inu muli bwino. Yesu Khristu wakuchizani inu. Ndizo PAKUTI ATERO MZIMU WOYERA.

118 Khalani ndi chikhulupiriro, ndipo mukhulupirire. Musati mukaikire. Basi mungokhulupirira. Kodi inu mungazindikire kupezekaponseponse kwa Ambuye Yesu? Zodabwitsa bwanji! Chavuta ndi chiyani?

119 Cha kuno apa pa ngodya, ine ndikuwona masomphenya. Adokotala sakudziwa kaya ndi khansa kapena TB. [Munthuyo akuti, "Kulondola kumeneko."—Mkonzi]. Izo nzoona. Koma

ngati inu mungakhulupirire izo, inu mwachiritsidwa, mulimonse. Chikhulupiriro chanu chakupulumutsani inu. Kazipitirirani.

120 Ndi zimenezotu. Kupezekaponseponse kwa Mulungu wamoyo! Ine ndikubetchera chikhulupiriro chanu. "Ngati inu mungakhulupirire!" Tsopano, Iye wauka kwa akufa. Iye ali pano ndi ife. Ndi Iyeyo! Ndizo zinthu zomwezo zimene Iye anazichita pamene Iye anali kuno pa dziko lapansi. Zaka thuu sauzande zadutsapo, Iye adakali moyobe, ndipo Iye ali wamoyo kwa nthawizonse. Mungokhulupirira, mukhale ndi chikhulupiriro.

121 Ine sindikukudziwani inu, dona. Ine sindinayambe ndakuwonanipo mmoyo wanga, sindikudziwa kalikonse ka inu. Izo nzoona, sichoncho inu? Yesu Khristu akukudziwani inu. Ngati Mulungu angawulule kwa ine chimene inu mwadzera pano, kodi inu mumukhulupirira Iye, ndipo mundikhulupirira ine kukhala mneneri Wake? Ngati Iye angachite zimenezo, inu mudziwa Chinachake chandizodza ine. Inu mukanayenera kudziwa kuti ndi Chimenecho. Tsopano ngati ine ndikanati, "Ine ndiika manja anga pa inu, muchiritsidwe," inu mukanakhala ndi ufulu wokaikira zimenezo. Koma ngati Mulungu angandiuze ine chinachake chimene inu mukudziwa kukhala choonadi, ndiye inu mukudziwa ngati icho chiri choonadi kapena ayi. Nkulondola uko? [Mlongo akuti, "Zoona zimenezo."—Mkonzi]. Ndi kusokonezeka kwachikazi. Munachitidwa opareshoni, ine ndikukuwonani inu mukuchokera pa tebulo la opareshoni, ndi chinachake choyera pa nkhope yanu, koma iyo siinayende bwino. Uko nkulondola. Koma, mdierekezi ameneyo anabisala kwa dokotala, koma iye sangakhoze kubisala kwa Mulungu. Pitani kunyumba, ndipo mukakhale bwino, dona, Yesu Khristu wakuchizani inu ndipo wakupangani inu kukhala bwino bwino.

Ngati inu mungakhulupirire!

122 Ndine mlendo kwa inu, dona. Kodi inu mukukhulupirira Yesu Khristu, Mwana wa Mulungu, ali pano? Kodi inu mukukhulupirira kuti Iye akuchizani inu? Matenda a shuga si kanthu, kuti Mulungu akuchiritseni. Kodi inu mukukhulupirira kuti Iye akuchiritsani inu? Ndiye kazipitani kwanu ndipo mukalandire machiritso anu mu Dzina la Yesu Khristu, Mwana wa Mulungu. Ameni.

Bwerani kuno, dona. Kodi inu mukukhulupirira?

123 Tsopano siyani kuganiza zimenezo kumbuyo uko! Izi si "kuwerenga maganizo." Iwe sungabisale ndi zimenezo tsopano! Ndiloleni ine ndikuwonetseni inu.

124 Ine sindikumudziwa mkazi uyu. Ikani dzanja lanu pa langa, dona. Ngati Mulungu angawulule kwa ine limene liri vuto lanu! Ine ndikuyang'ana mbali iyi, inu mukudziwa kuti ine sindikuwerenga malingaliro anu. Ngati Mulungu angawulule kwa ine limene liri vuto lanu, kodi inu mukhulupirira kuti Yesu

Khristu ndi Mwana wa Mulungu, ndipo ine kukhala wantchito Wake? Ngati inu mukutero, kwezani mmwamba dzanja lanu. Inu muli ndi vuto lachikazi, vuto lachidona. Uko nkulondola. Inu munali nalo; inu mulibe tsopano. Inu mwachiritsidwa. Pitani pa njira yanu, ndipo mukasangalale ndipo mukakondwere.

125 Bwerani, bwana. Vuto lakale la impsyo lija, ndi chinachake chikukuvutani inu. Kodi inu mukukhulupirira Mulungu akuchizani inu? [M'bale akuti, "Inde."—Mkonzi]. Kukuchizani inu kwa ilo? Ndiye, mu Dzina la Yesu Khristu, landirani machiritso anu, ndipo kazipitani pa njira yanu, mukusangalala. Ameni. Mulungu akudalitseni inu, m'bale.

Khulupirirani!

126 Inu muli bwanji, dona? Kodi inu simungakonde kuti muzipita, ndikukadya chakudya chabwino kenanso monga momwe inu munkachitira? Inu mwakhala muli wamanjenje, sichoncho inu? Zinapangitsa zilonda za mmimba kukhala mmimba mwanu. Pitani, mukatenge chitumbuwa ndipo mukadye, Yesu Khristu wakuchizani inu. Inu mupite panjira yanu, mukusangalala.

127 "Ngati inu mungakhulupirire!" Khalani ndi chikhulupiriro mwa Mulungu. Kodi inu mukukhulupirira? [Osonkhana akuti, "Ameni."—Mkonzi]. Wamoyo, Khristu wamphamvuzonse ali pano tsopano, kuti achiritse munthu aliyense ali muno.

128 Mphindi chabe. Kumbuyo uko kumusi kwa mzere, wakhala pansi pomwe apa, pakhala bambo wachichepere. Chikhulupiriro chako ndi chachikulu kuposa momwe iwe umaganizira kuti uli nacho, mwana. Iwe unali ndi vuto la mtima, sichoncho iwe? Ngati uko nkulondola, imirira pa mapazi ako. Yesu Khristu wakuchiritsa iwe, mwana. Iwe uli bwino. Kazipita pa njira yako, ndipo ukakhale bwino.

129 Kodi inu mukumukhulupirira Iye? [Osonkhana akuti, "Ameni."—Mkonzi]. Khalani ndi chikhulupiriro mwa Mulungu.

130 Apa pali bambo ine sindikumudziwa. Ife ndi alendo kwa wina ndi mzake. Ine ndikukhulupirira bambo uyu wabatizidwa mmawa uja. Koma ine sindikukudziwani inu, ndiribe lingaliro lokhudza inu. Nkulondola uko? Ngati Yesu Khristu atawulule kwa ine chimene inu mwabwerera pano, kodi inu mulandira izo?

131 Ndi angati mwa osonkhana ati alandire izo tsopano? [Osonkhana akuti, "Ameni."—Mkonzi]. "Ngati inu mungakhulupirire!" Mungokhala ndi chikhulupiriro. Musati mukaikire.

132 Bamboyo ali ndi vuto la khungu. Uko nkulondola. Ndipo ine ndikuwona inu mukutenga . . . Ndi vuto lachimuna, aponso. Uko nkulondola. Ngati ziri chomwecho, gwedezani dzanja lanu. Ndipo ine ndikuwona chinachake chakuda chaima pakati pa inu ndi mkazi; uyo ndi mkazi wanu. Inu mukumupempherera iye. Iye

ndi wochimwa, ndipo inu mukufuna kuti iye akhale Mkhristu. Ndizo PAKUTI ATERO AMBUYE. Uko nkulondola. Pitani, mukasanjike manja anu pa iye, ndipo mukamupempherere iye, kuti Mulungu Kumwamba akawulule kufunikira kwa zinthu izi kuti izo ndi zenizeni.

133 Kodi inu mukukhulupirira? Kodi inu mukukhulupirira kuti Mulungu achita izo? "Ngati inu mungakhulupirire!" Ine ndikuchibetchera chikhulupiriro chanu. Uko kumbuyo mmbuyo, paliponse pamene inu muli, yang'anani ndipo mukhale moyo! Khalani ndi chikhulupiriro mwa Mulungu, paliponse pamene inu muli. "Ngati inu mungakhulupirire, zinthu zonse ndi zotheka." Ngati inu mungakhulupirire! Penyani. Yang'anani mbali iyi. Pempherani. [M'bale Branham akuimikira—Mkonzi].

Inu mukuti, "Inu mukuyang'ana chiyani, M'bale Branham?"

134 Rebekah, bwerera mbali iyi pang'ono, wokondedwa. Ima pamene iwe ulipo. Apo pali mtsikana wanga wamng'ono, amene tsikulina adzakhala mneneri wamkazi, nayenso. Dona uyo waima apo pafupi ndi iwe, wokondedwa, wavala chipewa choyera, iye akuvutika ndi vuto la nkusani. Kwezani dzanja lanu, kapena imirirani pamapazi anu, dona. Inu mukupemphera kuti Mulungu akuitaneni, mundilole ine ndikuitaneni inu. Kulondola uko? Mulole mtsikana wanga wamng'ono ayike manja ake pa inu pamenepo. O Mulungu Wamuyaya, mu Dzina la Yesu Khristu, ine ndikudzudzula chiwanda chimenecho chimene chikumuvutitsa mkazi ameneyo. Ndipo mulole icho chichotsedwe, mu Dzina la Khristu. Ameni.

135 Oh, lodala likhale Dzina la Ambuye! Ambuye Yesu atadziwulula Iwoeni, nawonso. Kodi inu mukukhulupirira Iye ali pano? [Osonkhana akuti, "Ameni."—Mkonzi]. Ndiye mundilole ine ndikuuzeni inu, aliyense wa inu, pompano, ngati inu mungathe kukhulupirira izo, Yesu Khristu wakupangani aliyense wa inu kukhala bwino, pomwe pano. Ngati mawu anga ali owona *apa*, iwo ndi owona *apo*. Ngati inu mungachite zimene ine nditi ndikuuzeni inu kuti muchite, inu mukhoza kuchiritsidwa pomwe pano. Kodi inu mukukhulupirira izo? [Osonkhana akuti, "Ameni."] Ndiye ikani manja pa wina ndi mzake. Mungoika manja pa wina ndi mzake, mkati kapena kunja. Musati mukaikire! Ine ndamva mzimu wogontha ukusamuka. Apa Iye ali, Khristu woukitsidwa!

136 O Mulungu Wamuyaya ndi Wodala, mu Dzina la Ambuye Yesu, ine ndikuwutsutsa mzimu woipa uliwonse, mu Dzina la Khristu Ambuye, kuti iwo uchoke pa malo ano, utuluke mwa anthu awa. Ndipo mulole Mzimu Woyera waukulu tsopano umubatize aliyense muno, ndi chikhulupiriro chachikulu kuti tikhulupirire.

137 Oh, Satana, iwe chiwanda, iwe watinyengeza ife nthawi yaitali. Khristu waukitsidwa, Iye akuima pano ndi mafungulo a

imfa ndi gehena akulendewera pa Iye. Mphamvu ya machiritso yalipiridwa. Ndipo ife tikukulamulira iwe, mu Dzina la Yesu Khristu, Mwana wa Mulungu wamoyo, kuti iwe uchoke kwa anthu awa. Utuluke mwa iwo, Satana, kuti iwo apite ndipo akachiritsidwe.

138 Ngati inu mungakhulupirire ndi mtima wanu wonse, kuti Yesu Khristu wakuchizani inu, imirirani ku mapazi anu, ndipo mulandire mphamvu ya machiritso Auzimu ya Mulungu Wamphamvuzonse. Ndi zimenezotu! Ambuye alemekezeke! Ambuye adalitsidwe! Inu muli, mmodzi aliyense, wochiritsidwa. Imani pa mapazi anu, ndipo mumupatse Mulungu matamando! Ameni! Lodala likhale Dzina la Ambuye! Tiyeni timupatseni Iye matamando, pamene ife tikukweza manja athu ndi kumutamanda Iye. Dalitsani Mwana wa Mulungu wa moyo! Ameni!

Ndipo Maso Awo Anatseguka
Ndipo Iwo anamudziwa Iye CHA57-0421E
(And Their Eyes Were Opened And They Knew Him)

Uthenga uwu wa M'bale William Marrion Branham, woperekedwa mu Chingerezi Lamlungu la Isitara madzulo, Epulo 21, 1957, ku Branham Tabernacle ku Jeffersonville, Indiana, U.S.A., unatengedwa kuchokera pa matepi ojambulidwa ndi maginito nudindidwa mosachotsera mawu ena mu Chingerezi. Kumasulira kwa Chichewa uku kunadindidwa ndi kugawidwa ndi Voice Of God Recordings.

CHICHEWA

©2021 VGR, ALL RIGHTS RESERVED

Voice Of God Recordings, Malawi Office
P.O. Box 51453, Limbe, Malawi

Voice Of God Recordings
P.O. Box 950, Jeffersonville, Indiana 47131 U.S.A.
www.branham.org

Chidziwitso kwa ofuna kusindikiza

Maufulu onse ndi osungidwa. Bukhu ili mukhoza ku printa kunyumba kwanu ngati mutafuna kuti mugwiritse ntchito inuyo kapena kuti mukawapatse ena, ulere, ngati chida chofalitsira Uthenga wa Yesu Khristu. Bukhu ili simungathe kuligulitsa, kulichulukitsa kuti akhalepo ambiri, kuikidwa pa intaneti, kukaliika pakuti ena azitengapo, kumasuliridwa mu zinenero zina, kapena kugwiritsidwa ntchito ngati njira yopezera ndalama popanda chilolezo chochita kulembedwa ndi a Voice Of God Recordings®.

Ngati mukufuna kuti mumve zambiri kapena ngati mukufuna zipangizo zina zimene tiri nazo, chonde mulembere ku:

VOICE OF GOD RECORDINGS
P.O. BOX 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.
www.branham.org